UNGWIRO

. . .Ndipo kudzakhala pano ndi kudzapembedza limodzi ndi inu. Ndipo tsopano basi Uthenga usanati, ine ndiri naye mzanga wabwino pano pa nsanja usikuuno, Doctor Lee Vayle, wochokera ku First Baptist church ku Lima, Ohio, yemwe anali mmodzi wa wondithandizira wanga wa msonkhano wa ku Lima. Ine ndinamufunsa iye, akubwera kuno usikuuno, ngati iye angadzanene mawu chabe kwa osonkhana, mwinamwake okhudzana ndi msonkhano waku Lima, kwa mphindi yotsatira kapena ziwiri. Ndipo ndine woyamikira, wokondwera kukuwonetsani inu usikuuno, Doctor Lee Vayle, wachi Baptist wina amene ali ndi Mzimu Woyera.

2 [Mbale Lee Vayle akuyankhula kwa maminiti fortini, kuchitira umboni za anthu ambiri akuchiritsidwa.—Mkonzi.] Ameni. Mulungu akudalitseni inu, Mbale Vayle, nanunso.

3 Zimenezo zinali zonse zamphamvu kwa m'busa wa Baptist, sichoncho izo? Chabwino, ndife okondwa kwambiri kukhala ndi M'bale Vayle limodzi nafe. Ndipo ndithudi makomo ndi otseguka kuti iye adzabwerenso ndi kudzatichezera ife pa nthawi iliyonse imene iye angathe. Ndipo tsopano usikuuno . . .

Mawa usiku tidzakhala ndi—*Kuikidwammanda* kwa Ambuye Yesu.

4 Lamlungu mmawa tidzakhala ndi msonkhano wa sikisi koloko wa kutuluka kwa dzuwa. Ndipo ine ndikukhulupirira m'baleyo walengeza gawo lopitirira la msonkhanowu.

Tsopano tiyeni tipemphere mphindi chabe.

5 Ambuye wodala, Mawu Anu ali Choonadi, ndipo ife tiri othokoza chifukwa cha munthu yemwe amawagwira Iwo, mopanda mantha, pamene iwo akuwapereka Iwo kwa anthu. Ndipo pamene ife tikutsegula Baibulo usikuuno, kapena kusanthula masamba Ake, mulole Mzimu Woyera wodala ubwere ndipo udzatsegule Mawu a kumvetsa kwa ife. Kudzera mwa Yesu Khristu, ife tikupempha izi. Ameni.

6 Usiku wopambana uno umene ife tikukondwerera, wa kupachikidwa kwa Ambuye wathu wodala, ine ndikufuna kuti ndiwerenge usikuuno kuchokera ku milomo Yake Yomwe yofunika, Mawu amene Iye wakhala ali nawo atalembedwa mu Bukhu Lake. Mu Mateyu Woyera, mutu wa 4, ife . . . ndi ndime ya 47 ndi 48, ife tikuwerenga izi:

> *Ndipo ngati* inu *mulankhula ndi abale anu okha, mwachita chiyani* inu *choposa ena? kodi angakhale anthu akunja sachita chomwecho?*

Koma *chifukwa chake mukhale angwiro, ngakhale monga Atate anu akumwamba ali angwiro*.

7 Ndipo usikuuno ife tinaupereka kuti tiyankhule pa phunziro la *Ungwiro*. Tsopano ife . . . Umenewo ukuwoneka ngati mutu wachirendo kwambiri kuti tiwutenge kwa usiku wa kupachikidwa kwa Ambuye wathu. Koma lero, mwinamwake, inu mwakhala mukumvetsera pa wailesi, ndipo mwamva mauthenga osiyanasiyana ndi atumiki, momwe iwo analiperekera tsiku lowopsya lalikulu lija pamene Ambuye wathu anafera machimo a dziko lapansi. Chotero ine ndasankha, usikuuno, kuti ndipite mozungulira mwanjira yosiyana, kuti ndifike pa izo, kuti izo zikhoza kukhala zosiyaniranapo pang'ono ndipo zikhoza kukusisimutsani pang'ono. Ndipo mulole Mzimu Woyera wodala uwadzodze Mawu tsopano pamene ife tikutenga kuyesetsa kuti tiwabweretse Iwo.

8 Mulungu amafuna ungwiro. Ife tikufuna tizisunge izo mmalingaliro mwathu, kuti palibe chirichonse chatheka chimene chingathe kukafika mu Kukhalapo kwa Mulungu. Icho chiyenera kukhala changwiro, kupembedza kwathu, chirichonse.

9 Tsopano, mmunda wa Edeni, Mulungu anali ndi Adamu ndi Eva mmunda. Ndipo iwo anachimwa ndipo analakwira malamulo a Mulungu, pochimwa, kusamvera. Ndipo pamene kulakwa kubwera, kusamvera ndi kulakwira kwa lamulo. Ndipo lamulo la Mulungu, Iye pokhala woyera, basi woyera mosaipitsidwa, chotero palibe banga la chidetso lingaime konse mu Kukhalapo Kwake. Kotero, ngati tchimo linabwera mu dziko mwa kulakwa, ndiye tchimolo ayenera kuthana nalo wochimwayo asanadzaime konse mu Kukhalapo kwa Mulungu.

10 Tsopano, ngati palibepo lamulo, ndiye kuti palibenso chirungamo. Koma lamulo linkafuna, kapena, chirungamo chinkafuna lamulo. Ndipo lamulo, pamene ilo—ilo liitanidwa, ilo limatulutsa chirungamo.

11 Tsopano, mwa lamulo, palibe mnofu ungapulumutsidwe. Tsopano, lamulo silingathe kutipulumutsa ife. Lamulo linangokhala chinthu chimene chinatiika ife mu ndende, koma ilo liribe mphamvu yowombolera. Lamulo linkangotisonyeza ife kuti tinali ochimwa, ndipo limatitsutsa ife. Ndicho chimene lamulo limachita. Ndi kubweretsa chitsutso, kapena kukusonyezani inu pamene pali kulakwitsa kwanu. Kotero lamulo, pa lokha, silikanatha kupulumutsa. Ilo limangotha kutiimba mlandu.

12 Ndipo Mulungu, pokhala woyera ndi worungama, Iye ankayenera kukhala ndi kuimba mlandu. Iye ankayenera kuti amuimbe mlandu wochimwayo chifukwa iye anali atalumpha malire a chisomo, ndipo anali atakhala mzika yakuswa lamulo. Ndiye, iye ayenera kulangidwa.

13 Ndipo lamulo lirilonse limakhala nacho chilango, pakuti, chilango cha kulakwira lamulo la Mulungu ndi imfa. Ndipo ilo linkayenera kupereka imfa kwa mtundu wa anthu. Ndipo mtundu wonse wa anthu uli pansi pa chilango cha lamulo ili.

14 Tsopano, pamene Adamu ndi Eva anachimwa, apo panalibe njira, panalibe yankho lina kuti iwo akanatha konse kuima mu Kukhalapo kwa Mulungu kenanso, pokhapokhapo ngati tchimo ili atathana nalo. Ndipo palibe munthu amene angachite tchimo la mtundu uliwonse, ziribe kanthu kuti ndi laling'ono chotani kapena lalikulu chotani, tchimo limenelo palokha liyenera kuthetsedwa zisanafike pakuti amene analichitayo akaime konse mu Kukhalapo kwa Mulungu Woyera.

15 Chotero, pamenepo, pamene Adamu ndi Eva anachimwa ndipo anali atalakwira lamulo, iwo anali pansi pa imfa. Ndipo lamulo linkayenera kuti ligwire ntchito, chotero ilo linaika mtundu wonse wa anthu pansi pa chilango cha imfa. Tsopano ngati ife titakwanitsa kukhazikika kwa mphindi pang'ono tsopano, mu kuganiza kwathu, ndi kuyang'ana pa chithunzi chachikulu ichi, ndi kukumbukira kuti munthu aliyense pano akuphatikizidwa nawo mu zimenezi. Mwamuna ndi mkazi aliyense, mwana, akuphatikizidwa nawo mu chilango cha imfa, pamene analakwa mkulu wa mtundu wa anthu, Adamu; pamene iye anachimwa, wina aliyense wa ife tinakhala kapolo wa tchimo.

16 Ndipo tchimo ayenera kuthana nalo. Ndipo chotero, Mulungu, mu kupandamalire Kwake kwakukulu ndi chikondi Chake chachikulu . . . Lamulo linali lakuti limulekanitse wochimwa kuchoka kwa Womupanga wake; kenako iye nkudzathetsedwa, ndipo kuthetsedwa kwathunthu, apo sipakanadzakhala konse njira yoti iye abwerere nkomwe pokhapokhapo tchimo limenelo atathana nalo. Ndipo zikanakhala zophweka kwambiri pamenepo kukhulupirira mu kuthetsedwa kwathunthu kwa wochimwa pamapeto, pakuti iye walekanitsidwa kwathunthu, kwanthawizonse kuchoka mu Kukhalapo kwa Mulungu.

17 Tsopano zindikirani tchimo ili. Ndipo momwe Mulungu, pokhala wolungama, ndipo Iye sakanachita kanthu kalikonse koma kungokhala wolungama, pakuti Iye ndi gwero la chirungamo chonse, ndiye sipakanakhala chirichonse choti Iye achite koma kuika chilango cha kulakwa uku. Ndipo chilangocho chinali imfa, pakuti Iye anati, "Tsiku limene iwe udzadya zimenezo, tsiku limenelo iwe udzafa ndithu." Tsopano, ndi chithunzi chakuda chimene ife tiri nacho apa.

18 Komano ngati ife titangobwerera mmbuyo pang'ono, ndi kukafufuza zikhumbo zenizeni za Mulungu, Baibulo limatiuza mwachimvekere ife kuti "Mulungu ndi chikondi." Komabe, pokhala chikondi, Iye ayenera kukhala wolungama.

Chotero, chikondi sichimatanthauza basi chinthu chimene chitha kunyengerereredwa ndi kuseweretsedwa. Chikondi ndicho chirungamo cha Mulungu.

19 Tsopano, pamene Mulungu anawona kuti ana Ake anali atachimwira lamulo Lake, ndipo kuti iwo ankayenera kufa imfa, pamenepo chikondi cha pachokha chinalowererapo kuti chikapange njira. Pakuti, Mulungu anawona kuti ana awa anali oti mwamtheradi, athetsedwe kwathunthu kuchoka Pamaso Pake. Panalibe chirichonse chimene chikanachitidwa, pakuti iwo anali atachimwira lamulo Lake, ndipo chilango cha lamulo Lake chinali imfa.

20 Ndiyeno chikondi cha Mulungu chinatuluka kutsatira anthu Ake. Ndipo pamene chikondi Chaumulungu chiperekedwa, chisomo chochita mwachokha chimapereka chinthu cha chikondi. Ndipo Mulungu, mwa kudziwiratu, pamene Iye anawukonda mtundu Wake mwabwino kwambiri; komabe, anali ndi chilango, Iye anapangitsa imfa yoloweza mmalo kuti ikachitike mmunda wa Edeni. Izo zinali kuti, Iye analoweza mmalo cholengedwa chosalakwa, mwanawankhosa wamng'ono amene sankadziwa tchimo, ndipo izo zinapita kwa choloweza mmalo, kuti chikagwire ntchito ndi kukafa mmalo mwa wochimwa wolakwayo. Ndipo anali mwanawankhosa, wophedwa, kuti akagwirizize moyo wa mzika Zake.

21 Kudutsa mu Chipangano Chakale chonse iwo ankapereka magazi a anaankhosa ndi mbuzi, nkhosa, ng'ombe ndi ana a ng'ombe, imfa yoloweza mmalo. Koma, zonsezo mu chuma chachikulu cha Mulungu, kumbuyo kwa malingaliro Ake kunali kuli Chinthu chenichenicho chikubwera, chimene chikanadzakhala. Izo zinali mithunzi ya Chinthu chenichenicho chimene chinali choti chikubwera. Ndipo Chinthu chenicheni chinali choti chikubwera, chinali Mwana Wake yekhayo wokondedwa. Anaankhosa onse amene anafa anali mthunzi chabe. Ndipo mthunzi umangokhala mbali yotsukidwa ya chinthucho. Ndipo iwo ankangoyankhula za Kalvare kuti akubwera.

22 Tsopano kuti tikhale ndi chithunzi cha izi, tiyeni titembenuze mu Mabaibulo athu, ku Bukhu la Ahebri, ndipo titenge apa zimene Paulo, mtumwi wamkulu uja akuyankhula, akuyesera kuti atilekanitsire ife zinthu izi. Mu mutu wa 10 wa Bukhu la Ahebri, ife tikuwerenga izi.

23 Ndipo ine ndimangowakonda Mawu! Mawu ali Choonadi. Ndipo ine ndimakonda kuwawerenga Iwo pamaso pa gulu langa, chifukwa ine ndikudziwa kuti mu chiweruzo ine ndidzaima nawo iwo. Ndipo ine ndidzayenera kuti ndidzayankhire. Chotero ngati ine ndizibweretsa Izo kuchokera ku Mawu, ndiye ine sindidzakhala wolakwa; chifukwa Iwo ndi Mawu, ndipo Mulungu amakhala ndi choyankhira pa Mawu Ake.

24 Ife tikumawona zochuluka kwambiri lero, za avangeli ndi ena otero, kumangirizira pa anthu. Oh, ndi chinthu chamanyazi! Ndipo ife timapeza, tikapita mmatchalitchi, ife tikalowa mu tchalitchi ndipo iwe umapeza m'busa winawake, ali ndi kachitidwe kena kachirendo pa iye, kutengeka kwina pang'ono. Ngati iwe susamala, gulu lonselo litengera mzimu umenewo. Ngati iye akhala wotengeka pang'ono, kapena kumagwedeza mutu wake, kapena kanthu kena kachirendo kakang'ono, chabwino, tchalitchi chonsecho chitengera zimenezo. Ndipo ife tiri nazo, lero, mmatchalitchi athu amakono, kumene kumakhala zogirigisha ndi zinthu pang'ono monga choncho. Ndipo izo ziri ndi chisokonezo chotero! Koma, oh, abale anga okondedwa, ngati inayamba yakhalapo nthawi imene ife tiyenera kumakhala pa Mawu, ndi lero!

25 Inu mukuona, ine ndingadane nazo kudzaima pa chiweruzo ndi kumadziwa kuti ine ndinali ndi kenakake kakang'ono kosadalirika ka vumbulutso laling'ono lachirendo, ndipo ndinawasocheretsa anthu. Ine sindikufuna kuti iwo azikhala ndi mzimu wanga kapena zochita zanga, koma ine ndikufuna kuti iwo azikhala ndi Mzimu wa Mulungu mwa Mawu a Mulungu, zimenezo zimabereka Choonadi.

26 Kotero pa chochitika chachikulu ichi usikuuno, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera ku Mawu Amuyaya a Mulungu. Tsopano ife tikuzindikira kuti lamulo lakhalapo kwa zaka zambiri, koma lamulo silimatha konse kuchotsapo tchimo. Monga ine ndakhala ndikunenera mmbuyomu, ilo linangokhala nyumba ya undende. Ilo linali wofufuza wamkulu amene amakuuza iwe zimene unali utachita, koma samakhala ndi njira yokuwombolera iwe. Ilo limakuika iwe mu shopu yapinyolo, koma uko kunalibe Wowombola woti akutululutsemo iwe, limodzi ndi ilo. Ilo limangokuika iwe mu ndende, kungokudziwitsa iwe kuti unali wochimwa. Koma tsopano zindikirani mu Ahebri, mutu wa 10, pamene ife tikuwerenga.

> *Pakuti chilamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zirinkudza, ndipo osati chifaniziro chenichenicho . . .*

27 Kumbukirani, ilo linali mthunzi wa chifaniziro chakudza. Mthunzi umangowonetsera kuti pali chifaniziro chimene chikupanga mthunziwo. "Mthunzi wa zinthu zakudza, ndipo osati chifaniziro chenichenicho." Zindikirani, "wa zinthu . . . "

> *. . . chifaniziro chenicheni cha zinthu, sichikhoza ndi nsembe zimenezo zimene* zinali *kuperekedwa . . . mosalekeza kumupanga* wakudzayo kukhala *wangwiro.*

28 Tsopano, Mulungu, pachiyambi, ankafuna ungwiro. Yesu, pamene Iye anabwera padziko lapansi, anati, "Khalani inu angwiro, monga Mulungu Kumwamba ali wangwiro." Ndipo lamulo, pokhala nawo mthunzi wa zinthu zakudza, silimatha

konse kumupanga wopembedzayo wangwiro. Mukuchimvetsa chithunzicho? Tsopano tiyeni tipitenso pa izo kachiwiri kuchitira kuti mukhale otsimikiza kuti simunaziphonye izo. Mulungu amafuna chiyero changwiro. Palibe mmodzi yemwe angaime mu chifaniziro Chake, ali ndi kachidutswa kakang'ono kamodzi ka tchimo. Yesu anachitira umboni chomwecho, ndipo anati, "Khalani angwiro, chimodzimodzi monga Mulungu Kumwamba ali wangwiro."

29 Ndipo Baibulo linanena kuti, "Lamulo silimatha konse, ndi nsembe zake, kumupanga wobwerayo kukhala wangwiro." Ndiye, lamulo silimatha kupangitsa chirichonse kukhala changwiro. Ilo linangokhala cholozera. Nsembe izi, zopangidwa chaka ndi chaka, sizimatha nkomwe kumupanga wopembedzayo kukhala wangwiro. Chotero potero, panalibe mmodzi wa pansi pa lamulo, kapena kusunga kwa malamulo, kapena pansi pa mithunzi, amatha kukhala wangwiro.

Pakuti (ndime ya 2) *potero izo sibwenzi zitaleka* kuti *ziziperekedwa*? . . .

30 Ngati pali chirichonse chimene ine ndingathe kuchita kuti ndidzipange ndekha kukhala wangwiro Pamaso pa Mulungu, ndiye Khristu sankasowa kuti andifere ine. Ngati pali chinthu chimodzi chimene inu mungathe kuchita, chimene chingakuyenerezeni chirichonse Pamaso pa Mulungu, ndiye kuti Khristu anafa pachabe. Palibe kusunga kwa lamulo, palibe malingaliro achilamulo a inu, palibe chiyero chanu chanu, palibe zinthu zimene mungathe kuzisiya, kusiya kunama, kusiya kuba, kusiya kusuta fodya, kusiya kupita ku kanema, inu ndinu otaikabe. Palibe chimene chingachite zimenezo! Kujowina matchalitchi, mipingu, miyambo, maubatizo, madongosolo a mpingo, kuwerenga kwa tizikhulupiriro, kunena mapemphero, zinthu zonsezo sizingawerengedwe kanthu. Inu mwataika! Palibe chinthu chimodzi chimene inu mungathe kuchita mwa inu nokha, pakuti ndinu wochimwa pansi pa chitsutso. Ndipo palibepo njira iliyonse mwa inunokha, kapena kachikhulupiriro kalikonse, kapena chirichonse chimene inu mungathe kuchita kapena kuchiganizira, cha inueni, chimene chingakuyenerezeni chinthu chimodzi Pamaso pa Mulungu, chifukwa ndinu wochimwa kuyamba ndi kuyamba.

31 Ndipo Baibulo limanena, kuti ife tonse tinabadwa mu tchimo, tinawumbidwa mu kusaeruzika, tinabwera ku dziko tikunena mabodza. Ndipo Mulungu sakanamutenga munthu mmodzi kuti amufere mzake, chifukwa winayo ndi wochimwa basi chimodzimodzi ndi mzakeyo. Mu Kukhalapo kwa Mulungu, arkibishopu wobadwa mu dziko lino ndi wochimwa basi chimodzimodzi ndi chiledzelere chotsikitsitsa cha mu mzindawu. Wina sangathe kumutetezera mzake.

32 Chotero, Iye anatenga moyo wosalakwa wa chinyama, mwanawankhosa wamng'ono. Ndipo pansi pa Chipangano Chakale, lamulo linali lakuti, pamene munthu wachimwa, iye amabweretsa mwanawankhosa pa guwa. Ngati iye walakwira lirilonse la malamulo, iye amabweretsa mwanawankhosa ndipo amadzamuika iye pa guwa, iye amasanjika manja ake pa mwanawankhosayo ndipo iye amavomereza machimo ake, kuti iye walakwitsa ndipo wadziwa kuti walakwa. Za . . . ndipo anali . . . Lamulo linkafuna imfa. Ndipo iye ankabweretsa mwanawankhosa mmalo mwake. Ndipo pamene iye . . . Khosi la chinyama chaching'onocho limadulidwa, ndipo iyo imayamba kumenyetsa miyendo yake, ndi kumalira. Ngati inu munayamba mwamuwonapo mwanawankhosa akamazingidwa, kumakhala kulira komvetsa chisoni bwanji! Kanthu kakang'ono kosawukako kakuyesera kulira, ndipo mtsempha wake wawukulu ukudulidwa. Ndipo pamene iye akumenya matheche ndi kuphiriphitha, ndipo pamene iye akudziwongola, ndiye amaphiriphitha ndi kumalira. Ndipo magazi amakhavukira, iwo amasambitsa ubweya wake wawung'ono ndi manja a wopembedzayo.

33 Ndipo wopembedzayo pozindikira, chifukwa chochita chigololo, chifukwa cha kunama, kuba, chirichonse chimene kulakwa kwake kunali, kapena ngakhale kuganiza zoipa, chirichonse chimene icho chinali mu mthunzi wawung'ono, iye amakhala wolakwa, chifukwa icho chinali chirengedwe chake. Iye anali munthu wolakwa, osati mwinamwake mwakukhumba, koma mwachirengedwe iye amakhala wolakwa. Ndipo iye amayenera kuzindikira kuti mwanawankhosa wamng'ono wosalakwa uyu wafa mmalo mwake. Ndipo iye amakamvera chisoni kanthu kakang'onoko.

34 Koma munthuyo, mwamsanga mwanawankhosa akangofa, ali ndi magazi a mwanawankhosa mmanja mwake, iye amachoka mnyumbayo ali ndi chikhumbo chomwecho mu mtima mwake, chimene iye anali nacho pachiyambi. Bwanji? Chifukwa moyo umene unali mwa mwanawankhosa wamng'onoyo . . . Moyo umakhala mmagazi. Moyo wako umakhala mmagazi ako. Ife tikudziwa zimenezo. Ndipo moyo mmagazi a mwanawankhosa unali moyo wa chinyama, chotero pamene mitsempha yake yasweka ndipo moyo nkuchokamo mwa chinyamacho, iwo sumakhoza kubwerera kwa wopembedzayo, chifukwa wopembedzayo anali munthu.

35 Magazi amapanga chophimba, koma iwo samatha kutetezera mwangwiro; chifukwa munthuyo amachoka mchipindamo, ali ndi chikhumbo chomwecho choti akachimwe, chimodzimodzi monga iye anali nacho poyamba penipeni. Koma, pochita izi, iye amayang'ana mtsogolo ku nthawi yomwe pakanati padzakhale Mwanawankhosa wangwiro atabwera. Ndipo iye amazichita izo

pa nsembe yowotchedwa, chifukwa iyo inali njira yokhayo imene iye amaidziwa.

36 Kotero, inu mukuona, pamene magazi amatsanuliridwa, ndipo moyo nkumachoka mwa chinyama, iwo sumatha kubwereranso kwa munthuyo; pakuti, chinacho chinali chinyama, winayo anali munthu; chinyama chosalakwa, kupita kwa munthu wolakwa.

37 Koma, oh, tsiku lina, zaka thuu sauzande zapitazo, Mwanawankhosa wa Mulungu anabadwira modyera ziweto mwamung'ono uko ku Betelehemu, ndipo anatsogoleredwa ngati nkhosa akupita kokaphedwa kwake. Zaka naintini handiredi zina zapitazo, madzulo ano, pa firii koloko Iye anafa. Ndipo Mwanawankhosa wa Mulungu wopanda bangayo, wopanda chilema anapachikidwa pa mtanda wa Kalvare ndipo anafera wochimwa aliyense. Tsopano pamene wopembedza abwera kwa Mwanawankhosa uyu, mwa chikhulupiriro! Ndipo uyu ndi Mwanawankhosa wa mtundu wosiyana. Iye si Mwanawankhosa monga winayo.

38 Palibe munthu angathe kubwera kwa Mwanawankhosa uyu, kupatula Mulungu atamukoka iye poyamba. Inu mukuwona kuchita kwayekha kwa Mulungu? Oh, ine ndikuyembekeza izi zikulowerera mwakuya kwambiri tsopano. Penyani. Mulungu amadziwa kuti anali ndi nkhosa mu dziko lino. Iye ankadziwa kuti Iye adzakhala nawo anthu oti adzapulumutsidwe, ndipo chikondi Chake chinayang'ana pansi ndipo chinawawona iwo amene akanadzapulumutsidwa; chotero, mwakudziwiratu, Iye anawukonzeratu Mpingo kuti udzakumane naye Iye uko, wopanda banga kapena khwinya. Ndipo ngati Mulungu ankafuna Mpingo wopanda banga kapena khwinya, Iye amayenera kukhala ndi chinachake choti chidzapange izo mwanjira imeneyo. Iye sakanafuna izo, chirungamo Chake, ziweruzo Zake sizikanamulola Iye kuti afunse chinthu choterocho ngati pakanakhala popanda njira yopangira izo.

39 Ndipo munthu sangathe kuchita izo mwa iyeyekha. Iye ndi wolephera kwathunthu. Mulungu anamulola iye kuti aziwone izo kudzera mu lamulo, kudzera mwa oweruza, ndi kudzera mu Chipangano Chakale chonse. Iye anatumiza aneneri, Iye anatumiza munthu wolungama, ndipo iwo anapeza kuti mmodzi aliyense amalephera.

40 Chotero, Mulungu, mwa chisomo Chake cha mwayekha, anatumiza, kuchokera ku makonde a Ulemelero, Mwana Wake wobadwa yekhayo, kuti adzatenge malo athu.

41 Kumbukirani, ngati Iye akanati papa wa ku Roma atenge izo, iye sakanatha kuchita izo. Ngati Iye akanati arkibishopu waku Canterbury achite izo, iye sakanatha kuchita izo. Ngati Iye akanaitanitsa bambo woyera wolemekezeka kwambiri kapena bishopu wa mdziko, iye sakanatha kuchita izo. Iye basi

akanakanidwira kutali chimodzimodzi monga Yudasi Iskarioti anachitira. Iye sakanatha kuchita izo, chifukwa iye anali "wobadwa mu tchimo, wowumbidwa mu kusaeruzika, nabwera mdziko kumanena mabodza," ndipo wosowa chitetezero kwa iyemwini.

42 Aleluya! Koma apo panabwera Mmodzi kuchokera ku makonde aku Ulemelero; sanali winanso, osati munthu, osati munthu wabwino, osatinso Myuda kapena Wamitundu. Iye sanali china chotsikira pa Mulungu Wamphamvuzonse, anadzabisala mu mnofu wa munthu. Iye anabwera, Mwiniwake, kuti adzapereke Magazi Ake Omwe, pakuti Iwo sanabwere podzera nkugonana. Kugonana kunalibe kanthu kochita nazo izo. Koma Iye anamufungatira namwali, ndipo anabala khungu la Magazi limene Iye analilenga, Mwiniwake, Uyo wosalakwayo.

43 Ndiye chipulumutso changa, chanu, usikuuno, sichimakhazikika pa kukhoza kwa zochita zathu zathu. Icho chimakhazikika pa chisomo chovomerezeka chapayekha cha Mulungu Wamphamvuzonse Amene anatisankha ife mwa Iye. Ndithudi. Ine sindingathe kukhala wangwiro, ngakhalenso inu simungathe kukhala wangwiro. Ndipo ife sitimadzinenera kuti ndife angwiro. Koma ife tiri nacho chitonthozo chimodzi ichi, kuti, chikhulupiriro chathu chimatsamira pa Nsembe yangwiro imene inalandiridwa kale!

44 Ndiye ife tingadziwe bwanji kuti tiri nacho Icho? Pamene wopembedza ayika manja ake, mwa chikhulupiriro, pa thupi la Ambuye Yesu, ndipo namverera kuwawa kwa tchimo, ndi mnyozo wa malovu pa nkhope yake yomwe, akamamverera kubuula kwa Getsemane, zowawa za Kalvare, ndipo nkumadziwa kuti iye ndi wolakwa, ndipo nkumavomereza machimo ake molondola, "O Ambuye Wodala, ndine wolakwa. Ndipo ndiribe njira ina koma Inu kuti mundithandize ine. Ndipo mwa chikhulupiriro . . . Inu mukuitana, Mzimu Woyera, wabwera ndipo ukundiitana ine kuti bwera. Ndipo ine tsopano, mwa chikhulupiriro, ndikumuvomereza Yesu ngati Mpulumutsi wanga wanga." Moyo uwo umene unabwera kuchokera kwa Iye pa Kalvare, wotchedwa Mzimu Woyera, umene unadzabisidwa mu khungu la Magazi la Ambuye Yesu, umabwerera kwa wopembedzayo ndipo umadzamubatiza iye ndi Mzimu Woyera, kumulowetsa mu Thupi la Khristu.

45 Ndipo Iye anaweruzidwa kale. Inu simukusowa kuti muzidandaula za chiweruzo. Pamene ine ndipotoloka ndi kuyang'ana pa mtanda wawung'ono uwo, ine ndimazindikira zimenezo, kuti iwo ukuimira thupi Lake. Ndipo tsopano thupi limenelo linaweruzidwa kale. Mulungu sangathenso kuliweruza ilo mwachirungamo kachiwiri, pakuti ilo laweruzidwa kale. Mulungu anakantha ziweruzo za imfa pa thupi limenelo. Ndipo bola ngati ine nditapeza njira yoti ndikabisale mu thupi limenelo! Chiweruzo Chake chinakantha mmalo mwa ine ndi

inu. Ife tiri amfulu! Aroma 8:1, amati, "Kotero palibe kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene sayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu." Ndi zimenezotu, palibe kutsutsika! Ine sindikusamala chobwera kapena chopita, inu mwabisala pansi pa Magazi.

46 Chinanso, timalowa chotani Mthupi limenelo? Akorinto Woyamba 12:13, amanena kuti, "Mwa Mzimu umodzi!" Kodi Mzimu umabwera chotani? Kudzera mwa Nsembe. Kodi Mzimu umakhala kuti? Mkati mwa Magazi. Nchifukwa chiyani chinyama sichimabwerera? Icho chinali chinyama. Mzimu wa chinyama sukanatha kubwerera pa mzimu wa munthu ndi kuchita chirichonse kwa iwo, chifukwa mzimu wa munthu unali mzere wapamwamba wa moyo kuposa wa chinyama. Koma palibe mzimu wa munthu wina ukanatha kubwerera. Ngati inu muli ndi mzimu wa makolo ena, izo ndi zamizimu. Koma Mulungu Mwiniwake anabwera, kuti Mzimu Wake Womwe, umene uli mzere wapamwamba wa mzimu umene ulipo, udzakhoze kubwerera mmawonekedwe a ubatizo wa Mzimu Woyera, kupita kwa wopembedzayo, kudzera Mmagazi a Khristu, ndi kumutengera iye kukalowa mu Thupi. Iye ali wotetezeka!

47 Penyani. Magazi a ng'ombe ndi mbuzi sakanagwira ntchito, powona kuti iwo anali ofooka. Tsopano tiyeni tiyambe kuwerenga, pafupifupi ndime ya 12. Chabwino. Magazi a ng'ombe ndi mbuzi sakanatha kugwira ntchito, sakanakhozanso kutetezera. Penyani.

> *Koma munthu uyu,* (Munthu wake uti? Bishopu? Ayi. Papa? Ayi.)...
>
> *Koma munthu uyu, iye atatha...atapereka nsembe imodzi kwa* tchimo *kwa nthawizonse, anadzakhala pansi* pa *dzanja lamanja la Mulungu;*
>
> *Kuyambira pamenepo kuyembekezera mpaka adani ake atapangidwa kukhala chopondera chake.*

48 Kodi inu mwakonzeka? Kodi inu mwakonzekera Mawu? Mvetserani kwa Izi, ndiye ine ndikufuna kuti inu muzilole Izo zizame mwakuya. Mvetserani mwatcheru.

> *Pakuti ndi nsembe imodzi (*osati ya chaka ndi chaka, osati chitsitsimutso pambuyo pa chitsitsimutso, osati msonkhano pambuyo pa msonkhano, osati tsiku pambuyo pa tsiku)...
>
> Koma *mwa nsembe imodzi iye* watipanga a-n-g-w-i-r-o (iwo atero? Iye watero!)...
>
> *...mwa nsembe imodzi iye* watipanga *angwiro* (chimenecho ndicho chofuna cha Mulungu) *kwa nthawizonse iwo amene ayeretsedwa.*

49 Ndi zimenezotu. Ndiro yankho kwa imfa ya Khristu. Ndiro yankho kwa Kalvare. Iye mwamtheradi, ndi Magazi Ake Omwe, anagula machimo athu, ndipo anatipanga angwiro kwanthawizonse, okhulupirira Ake. Chotero, mwa Khristu ife timaima opandachilema, timapangidwa angwiro mu Kukhalapo kwa Mulungu Wamphamvuzonse. Ife timakhala anthu opandachodalira, ndi ziphunzitso zathu; ife tonse timaphunzitsidwa kuti ife tiyenera kufika pa malo ena, ife tiyenera kuchita chinthu chinachake. Ayi, m'bale wanga, si chimene inu mwachita; ndi chimene Mulungu anakuchitirani inu! Ife timakhala tsopano, ngati ife tilungamitsidwa mwa chikhulupiriro, ife timapangidwa kukhala angwiro mu Kukhalapo kwa Mulungu.

50 Ndiye Yesu anati, "Khalani inu chotero angwiro." Ndiye, izo zinapangidwa zangwiro kwa nthawizonse. Mulungu, kudzera mu imfa ya Khristu, zaka naintini handiredi zapitazo, lero, anampanga wokhulupirira kukhala wangwiro, yemwe Iye anamuwoneratu chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, kwanthawizonse. Ndipo iwo amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa. "Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana; iwo amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa; iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa kale ulemerelo." Iye anawapanga kukhala angwiro okhulupirira Ake!

51 Tsopano penyani, tiyeni tibwerere mmbuyo tsopano ku ndime ya 1.

> *. . . lamulo pokhala nawo mthunzi wa zinthu zabwino zakudza, ndipo osati chifaniziro chenicheni cha zinthu* zimenezo*, sizingatheke ndi nsembe zimenezo* zimene *zimaperekedwa chaka ndi chaka mosalekeza kumupanga* wobwerayo kukhala *wangwiro.*

52 Penyani "ungwiro," ndi zimene ife tikuyankhulapo.

> *Chifukwa potero* izo sibwenzi *zitasiya kuperekedwa? chifukwa chakuti* wopembedzayo *akatsukidwa kamodzi* sibwenzi *akukhalanso ndi kukumbukira kwa* tchimo.

53 Kodi inu mukutanthauza chiyani? Mawu akuti *kukumbukira* pamenepo, ndipo kutanthauzira, kolondola, ndi "chokhumba." Ndipo ngati munthu abwera, wopembedzayo, molondola, pamaso pa Khristu, powona kuzunzika Kwake, ndipo iye nkudzipereka yekha kwa Khristu, ndi kuti, "O Ambuye Mulungu, mulibemo kalikonse mwa ine kamene kangatetezere, koma ine kwathunthu ndikudalira pa Inu," ndiye Mzimu Woyera umenewo umabwera mu mtima wa munthuyo, funso kumene la tchimo limakonzedwa kwanthawizonse, chifukwa chikhumbo chirichonse cha tchimo chachotsedwa mwa inu. Pakuti ngati lamulo likanakhoza kuchita zimenezo, nsembe zimenezo sibwenzi zitasiya; koma pokhala kuti ilo silimatha kuchita

zimenezo, Khristu ankayenera kuti adzafe, kuti adzatipange ife kukhala angwiro.

54 Abwenzi, pali zinthu zambiri zimene ife tikanatha kunena usikuuno, zokhudza ungwiro. Ife nthawizonse timakhala tikuyesetsa kukolowola maso a mzathu, kuti tidzipange tokha kukhala oyera pang'ono kuposa iwowo—iwowo. Koma ngati ife tikanangoyang'ana pa chithunzi, ndi chisomo chabe cha Mulungu kuti ife tiri chimene ife tiri.

55 Kuno nthawiina kale, mu Ohio, ine ndinaphunzira phunziro mwanjira yovuta. Ine ndimachititsa msonkhano uko ku Ohio, ndipo ine ndimakhalira ku midzi. Chifukwa cha kuchuluka kwa anthu, ine sindikanatha kuti ndizikhala mu mzinda.

56 Ife tinali tikudya pa malo odyera a Dunkard. Ndipo operekera zakudya okondeka achichepere awo, ndiponso wovala bwino, ndipo awukhondo monga iwo akanakhalira, owoneka mwaudona, amatumikira pa ife. Ako kanali kamalo kakang'ono ka kumwamba, kudya pa malo oterowo. Kitchini yawo inali yawukhondo kwambiri. Ndipo Lamlungu iwo ankatseka ndi kupita ku tchalitchi chawo. Ine ndinali ndi njala pang'ono, ine ndinali ndikupita kuti ndikalalikire Lamlungu madzulo.

57 Ndipo ine ndinapita kwa aang'ono awamba. . . basi malo odyera a achisawawa achi Amerika, kuti ndikapeze chinachake choti ndidye. Ndipo pamene ine ndinalowa pakhomo, kodi ine ndinamva chiyani koma makina ochitira njuga akulira! Ndipo anali ataima pamenepo bambo wa usinkhu wanga, amene mwinamwake anali wokwatira, ali ndi nkono wake atamukumbatira mkazi, akusewera makina ochitira njuga. Lamulo lathu lomwe, chitetezero cha chirungamo chathu, cha katundu wathu, anali ataima pamenepo akuphwanya chinthu kumene chimene iye amayenera kuti azichitetezera. Chifukwa, ndi zoletsedwa kuchita njuga mu Ohio, kusewera makina ochitira njuga.

58 Ndipo ine ndinapotoloka ndipo ndinayang'ana kumbuyo kwa nyumbayo, pamenepo panali gulu la achinyamata a mzaka za mmatini, ndi marekodi akale a gwedemula ali pa makina, akuimba. Dona wamng'ono wa pafupifupi usinkhu wa zaka eyitini, wowoneka bwino mmawumbidwe ake ngati mkazi. Koma iye anali ataima pamenepo ndi diresi lake lalifupi kumaso, ndipo mmodzi wa anyamatawo anali ndi manja ake pa mtsikanayo, komwe iwo samayenera kukhala. Ndipo iwo anali akusuta ndi kumwa.

Ndipo ine ndinaganiza, "O Mulungu, Inu mukutha bwanji kupirira zimenezo?"

59 Ndipo ine ndinayang'ana kumanja kwanga, pamene ine ndinamva winawake akupanga kubuula kwakukulu. Ndipo apo panakhala mkazi wokalamba, mwinamwake zaka sikisite, kapena sevente zakubadwa. Iye anali atavala zovala zakale

zazing'ono zopanda makhalidwe zija, basi pafupifupi theka mmwamba mwa miyendo yake, ndipo thupi lake lakale la makwinya linali basi lokhutchuka monga mmene ilo likanakhalira. Ndipo iye anali atazipaka izi apa zozipenta za mmilomo, ndipo chinthu chachikulu chofiira kumbali ya nkhope yake, atazipenta; atavala nsapato zazing'ono, sandasi, ali ndi zikhadabo za kuphazi zofiira, atazipenta; zikhadabo zofiira, atazipenta. Ndipo tsitsi lake anali atalidulira pansi kwambiri, ndipo atalinyolola, ndipo atalidaya mwa buluu. Ndipo ine ndinamuyang'ana iye.

60 Ndipo mbali ina ya tebuloyo panakhala amuna awiri, ataledzera. Mmodzi wa iwo (iyo inali nthawi ya chirimwe) atavala chikhotho chakale chachikulu cha ku nkhondo, ali ndi mpango wotuwa atawukulunga mkhosi mwake, ndipo manyenje ali ponseponse pa nkhope yake, akugeya ndipo akupitirira. Ndipo iwo anachokapo, mwamunayo anatero, kwa mkaziyo, ndipo anayamba kumayenda monga *chonchi,* akupita kokadzithandizira.

61 Ine ndinaima pamenepo. Ndipo ine ndinati, "Mulungu, chifukwa chiyani Inu simukuwononga chinthu chonsecho? Chifukwa chiyani Inu simukungochimiza icho pansi pa nthaka?" Ine ndinati, "Kodi Sarah wanga wamng'ono ndi Rebekah adzakula pansi pa zinthu ngati zimenezo?" Ine ndinati, "Zikutheka bwanji Inu, Mulungu, mu chiyero Chanu chachikulu, kuti mukupirira ndi kumayang'ana chinthu ngati chimenecho, ndipo osatumiza chivomezi ndi kuchimiza icho?"

62 Ndipo pamene ine ndinali nditaima pamenepo, ndikumuweruza mkaziyo, pamene ine ndimatero, ine ndinabwerera mmbuyo kuseri kwa chitseko. Ine ndinamverera Mzimu wa Mulungu utabwera pa ine, ndipo ine ndinapita kuseri kwa chitseko.

63 Ndipo ine ndinawona ngati chinachake chikuchita kamvuluvulu. Ndipo pamene icho chimatero, mu masomphenyawo, ilo linali dziko likuzungulira zungulira. Ndipo pamene ine ndinayang'ana, kuzungulira dziko panali kamzere kofiira, kuzungulira dziko. Ndipo pamene ine ndinafika kwa dzikolo, ine ndinadziwona ndekha, ndiri mnyamata wamng'ono, ndikuchita zinthu zimene ine sindimayenera kuti ndizichita; mwinamwake osati monga *chomwecho*, koma ilo linali tchimo. Ndipo nthawi iliyonse imene ine ndichita chirichonse, ine ndimawona mthunzi wawukulu wakuda uwo ukupita Kumwamba. Chimene, Mulungu bwenzi atandipha ine pa miniti imeneyo.

64 Ndiye ine ndinawona pataima pakati pa ine ndi Mulungu, panaima Nsembe yangwiro ija. Ine ndinamuwona Iye ataima pamenepo ali ndi minga pa mutu Wake, ndi malovu akuyenderera pa nkhope Yake. Ndipo nthawi iliyonse machimo

anga akayamba kumapita kwa Mulungu, Iye amakhoza kufikira ndi kuwagwira iwo, ngati bampala yapa galimoto. Iye anali akunditetezera ine ku imfa. Ndipo nthawi iliyonse ine ndikachita chirichonse cholakwika, Mulungu akanati andiphe ine. Ndithudi, chiyero Chake chimafuna zimenezo. Lamulo lake limafuna zimenezo. Ndipo nthawi iliyonse ine ndikachita chirichonse, kapena inu mukachita chirichonse, Magazi a Yesu Khristu amachita ngati bampala. Ndipo ine ndinawona kachingwe kofiira ako kamatanthauza zimenezo, potero, Magazi amaligwirizizabe dziko lapansi.

65 Ndipo pamene ine ndinaima, ndikuyang'ana, ine ndinayandikira pafupi pang'ono kwa Iye pamene ine ndimamuyang'ana Iye. Ndipo ine ndimatha kumumva Iye akuti, "Atate, mukhululukireni iye, iye sakudziwa chimene iye akuchita." Ndipo ine ndinayang'ana pansi, ndipo pamenepo panali bukhu. Ndipo panali Mngelo wolembera pamenepo, ndipo ataima pambali Pake. Ndipo nthawi iliyonse ine ndikachimwa, izo zimalembedwa pa bukhulo. Ndipo dzina langa linali pamenepo. Ndipo ine ndinazindikira kuti tsiku lina, ine . . . chingwe cha Magazi chimenecho chidzachotsedwapo ndipo ine ndidzayenera kuti ndidzakaime Pamaso pa Mulungu, ndi moyo wanga wochimwa. Koma, ine ndinawona, mwa chifundo Chake Iye amaletsetsa chiweruzo changa.

66 Ine ndinapita kwa Iye, modzichepetsa. Ine ndinagwada pa mawondo anga, ndipo ine ndinati, "O Yesu, Inu Mwana wa Mulungu, ndine wosayenera kuti ndibwere Pamaso Panu. Koma kodi Inu mungandikhululukire ine chifukwa cha zimene ine ndachita?"

67 Iye anakhudza kumbali Yake ndi dzanja Lake, anatenga bukhu lakalelo ndipo analembapo "wakhululukidwa" pa ilo, analiponyeranso ilo kumbuyo Kwake, ndipo machimo anga anali atapita! Kenako Iye anandiyang'ana ine, mwaukali mmaso, Iye anati, "Tsopano Ine ndakukhululukira iwe, koma iwe ukufuna kuti umuweruze iye." Zitatero ine ndinawona chimene chimatanthauza.

68 Pamene ine ndinachoka mmasomphenyawo, ine ndinayenda kupita kwa iye. Ine ndinati, "Inu muli bwanji?"

69 Iye anali akumwa. Iye anandiyang'ana ine mokweza, ndipo iye anati, "Oh, moni."

Ine ndinati, "Kodi ine ndingakhale pansi?"

Iye anati, "Ine ndapeza mzanga."

70 Ine ndinati, "Ine sindikutanthauza izo mwanjira imeneyo, dona. Ine ndikungofuna kuti ndiyankhule ndi inu, miniti."

Iye anati, "Khalani."

71 Ndipo ine ndinati, "Dona, maminiti pang'ono apitawo, nditaima patali kuseri kwa chitsekocho . . ." Ine ndinayamba

kumuuza iye. Ndipo pamene ine ndinayamba kuyang'ana, misozi inayamba kutsikira mmasaya ake. Ndipo iye anandiuza ine. . . ine ndinati, "Dona, inu simukuyenera kuti muzichita zinthu zimenezi. Yesu anafa, ndipo ziweruzo za Mulungu zimatchinjirizidwa ndi Magazi Ake. Inu simukuyenera kuti muzichita izi."

72 Ndipo iye anati, "Ayi, bwana." Iye anati, "Bambo anga anali dikoni mu tchalitchi. Ine ndinaleredwa mu nyumba ya Chikhristu. Mwamuna wanga ndi ine tinali mamembala a charter, ndipo tinkakhala moyo wa Chikhristu." Iye anayamba kundiuza ine, pambuyo pa imfa yake. . . Iye anali ndi atsikana aang'ono awiri, ndipo iye anasochera. Ndipo momwe atsikanawo anamuchokera iye, ndipo iye anali atawutaya moyo wake. Ndipo iye ankaganiza kuti panalibe konse chiyembekezo pa iye.

73 Koma ine ndinati, "Mulungu, achite chifundo! 'Iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana.'"

Iye anati, "Kodi ndinu M'busa Branham, wochokera kumusi uko?"

Ine ndinati, "Ndi ineyo."

74 Iye anati, "Ine ndikuzichitira ndekha manyazi, kuti ndakhala pano monga chonchi." Iye anati, "Kodi inu mukuganiza kuti pangakhale mwayi kwa ine?"

75 Ine ndinati, "Yesu mikono Yake ndi yotambasula, akudikirira kuti iwe ubwere, dona." Ndipo anthu enawo anayamba kutengeka. Ndipo ine ndinati, "Kodi iwe ungayende kutuluka ndi ine pansi apa?"

Iye anati, "ine nditero, bwana."

76 Ine ndinamugwira iye pa dzanja. Ine ndinati, "Ndiwe pafupifupi usinkhu wa amayi anga. Kodi iwe ungagwade pano ndi ine, pansipa?" Ndipo pamenepo pansi, ife tinaphokosera pa malo amenewo madzulo awo, ku msonkhano wa kachitidwe-kachikale. Ndipo Mulungu anamupulumutsa mkazi ameneyo, mwa chisomo Chake. Iye anadziveka yekha ndipo anabwera ku msonkhanowo, ndipo, mmene ine ndikudziwira, akukhala moyo wa Chikhristu usikuuno.

77 Ndi chiyani icho? Oh, Mulungu amafuna ungwiro! Iye amafuna kulapa kwanu. Iye amafuna kukhulupirika kwanu kwa Iye. Koma Iye akuyang'ana usikuuno. Ziribe kanthu kuti inu mwachimwa mochuluka bwanji, mochepa bwanji kapena mochuluka bwanji, inu ndinu wochimwabe, ndipo simungathe kukalowa mwanjira yina koma mwa Yesu Khristu, Nsembe yokwanira-zonse ya Mulungu. Ndipo mwa Iye inu mumakhala angwiro kwanthawizonse. Taganizani za zimenezo! Si kanthu kalikonse kamene inu mumachita. Si masamba atsopano amene inu mumatsegula. Si moyo watsopano umene inu mwawuyamba. Ndi kuvomereza kwa kulakwitsa kwanu, ndi chisomo cha

Mulungu kwa inu. Zimenezo zimakubweretsani inu ku ungwiro, ndipo mukatero inu mumapangidwa wangwiro mwa Yesu Khristu.

78 Ine ndikudalira, usikuuno, mzanga wa ine, pamene ife tiri pano pa nthawi yayikulu yofunika iyi tsopano, pamene zigamulo ziyenera kupangidwa mutatha kumva nkhani iyi. Inu zikhoza kutheka kuti inu simunayambe mwaimvapo iyo. Koma inu simungatuluke pa limodzi la makomo awo munthu yemweyo amene munalowa muno, inu muyenera kutuluka apo muli wabwinoko kapena woyipa.

79 Ndipo pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kamphindi chabe, ine ndikufuna kuti inu mulingalire mwamphamvu za izo. Nanga bwanji moyo wanu usikuuno? Yesu Khristu anakuferani inu.

80 Inu mukuti, "M'bale Branham, pamene ine ndidzasiye kusuta, pamene ine ndidzasiye kumwa, pamene ine ndidzachikonze chinthu ichi, ine ndidzachita zimenezo." Oh, izo sizidzachitidwa molondola. Inu simudzatha konse kuti mudzachite zimenezo. Bwanji inu osangobwera momwe inu mulirimo? Ndipo, mwa chikhulupiriro, mupite ku Mtsinje umenewo, mabala anu owukha akupereka, ndiye chikondi chowombola chidzakhale nyimbo yanu, ndipo idzakhala mpaka inu mudzafe.

81 Mukutengeranji choloweza mmalo? Mukuyeseranji kuti mukalowe pogwiritsa ntchito mpingo wanu? Mukuyeseranji kuti mulowe chifukwa chakuti inu munasiya kumwa kapena kusiya kunama? Mubwere mwanjira ya ungwiro! "Pakuti, mwa Nsembe imodzi, Iye wawapanga angwiro kwanthawizonse iwo amene ayeretsedwa."

"Kodi ine ndimayeretsedwa chotani?"

82 Muvomereze machimo anu Pamaso pa Magazi a Yesu; ndipo Moyo woturuka kuchokera ku Magazi amenewo, umabwereranso kwa wopembedzayo, ndipo umamuyeretsa iye ku zikhumbo za zinthu za mdziko. Pakuti, mwa Nsembe yokwanira mu zonseyo, Iye anatiyeretsa ife; Mzimu umodzi, ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi. "Tsopano palibenso kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, kwa iwo amene sayenda monga mwa thupi, koma Mzimu." Ngati inu mukuyesera kuti muziyenda mwa Mzimu, ndipo nkumasilirabe za thupi, Nsembeyo sinaiikidwe mokwanira kwa inu. Koma wopembedzayo akatsukidwa kamodzi, samakhalanso ndi chikhumbo cha tchimo.

83 Zimenezo zinali Kalvare. Iwo si malo okagulitsirako maluwa, kapena malo aang'ono okachitirako *izi* kapena *izo*. Iwo anali malo amene Mulungu ndi munthu anayanjanitsidwako. Iwo anali malo amene mtendere ndi chitetezero changwiro zinabweretsedwa kwa mtundu wa munthu. Kodi inu mungathe

kupita nane, usikuuno, mzanga wochimwa, ku Kalvare, ndipo mwa chikhulupiriro mukaike Magazi awa ku moyo wanu womwe, ndi kulola Mzimu Woyera ubwere ndi kudzakuyeretsani inu mwa Nsembe Yake yaikulu?

84 Ife tisanapemphere, kodi inu mungakweze dzanja lanu kwa Mulungu, ndikuti, "Mundichitire ine chifundo, Mulungu. Ine tsopano ndikuvomereza machimo anga onse, usiku wa Good Friday uno. Ndipo ine ndikuyamikira kuzunzika kwakukulu kumene Khristu anandichitira ine. Ine tsopano ndikupereka chifuniro changa chomwe, zolinga zanga zomwe ndi chirichonse, kuti ndikutsatireni Inu kuyambira lero, mpakana." Kodi inu mungakweze dzanja lanu, ndikuti, "Mundikumbukire ine, M'bale Branham, mu pemphero. Ndicho chigamulo cha mtima wanga"? Kodi alipo aliyense, usiku wopambana uno, pamene ife tikudikirira mphindi chabe? Cha apa kudzanja langa lamanja, ndithudi alipo mmodzi cha kumeneko. Kodi inu mukuchita manyazi ndi machimo anu? Kodi inu mukuchita manyazi ndi zimene inu mwachita?

85 Dziko usikuuno likufunafuna ngwazi. Ndipo ilo liri nazo ngwazi, kuyankhula mwathupi.

86 Tsiku lina mu Switzerland, pamene Swiss Switzerland anali pa chiwopsyezo, gulu laling'ono la ku Swiss linali litasonkhana mminda, kukatetezera—kukatetezera chuma chawo. Ankhondo aakulu amene amabwera anali atawakulira kwambiri iwo; iwo onse anali ophunzitsidwa, anali ndi mikondo yaikulu ndi zishango. Achi Swiss sakanatha kuchita kanthu koma kugonjera. Iwo anali ndi phiri kumbuyo kwawo. Ndiye uko kunali ngwazi amene anadzipereka. Winawake ankayenera kuti afe. Ndipo ngati iwo aluza nkhondoyo . . .

87 Iwo analibe kanthu koma mipeni yakale ya zikwakwa, ndi miyala, ndodo, zoti amenyere nazo. Pamene, ankhondo amene amabwerawo amawoneka ngati khoma la njerwa. Ngati iwo atati atengedwa, azikazi awo okondedwa achichepere akanagwiriridwa, atsikana awo aang'ono akanagwiriridwa, makanda awo akanaphedwa, mitu yawo ikanaphulitsidwa, nyumba zawo zikanapita, chirichonse chikanataika.

88 Ndiye uko kunali munthu, amene dzina lake likuiwalidwa mwamsanga, dzina lake ndi Arnold von Winkelried. Iye anadzipereka, ndipo anati, "Amuna a Switzerland, lero ine ndikupereka moyo wanga chifukwa cha Switzerland." Iye anati, "Basi kutsidya kwa phiri uko kuli nyumba yoyera yaing'ono. Ine ndiri ndi mkazi ndi ana atatu akundidikirira ine. Koma iwo sadzandiwonanso ine, pakuti, lero ine ndikupereka moyo wanga chifukwa cha Switzerland."

Iwo anati, "Kodi iwe uchita chiyani, Arnold von Winkelried?"

89 Iye anati, “Munditsatire ine, ndipo muchite zopambana zimene inu mungathe ndi zimene muli nazo zoti muchitire nazo.”

90 Ndipo iye anayang’ana pa ankhondowo mpaka iye anapeza pamene panali mikondo itawirira. Ndiye iye anakwezera manja ake mmwamba, iye anathamangira kumene kunali khoma la njerwa ya mikondo, ndipo anafuula, “Ndikupanga njira kwa ufulu! Ndikupanga njira kwa ufulu!” Mikondo handiredi inapotoloka kuti imubaye pamene iye amabwera; iye anatambasula mikono yake ndipo anaibayira iyo mchifuwa chake chomwe, yomwe inamubaira iye pansi, ndipo iye anafera pa nsonga za mikondo imeneyo. Achi Swiss awo anamutsatira iye ndi zibonga ndi ndodo. Kuwonetsera kopambana kuja kwa ungwazi kunasokoneza ankhondo amenewo, mpaka achi Swiss anawamenya iwo kuwathamangitsa mdzikolo. Ndipo iwo sanakhalenso ndi nkhondo kuyambira tsiku limenelo, chiyambireni.

91 Mukaimirira mu Switzerland ndipo mukatchula dzina la Arnold von Winkelried, inu mudzawona misonzi ikuyenderera mmasaya mwawo. Chifukwa chiyani? Iye anapulumutsa dziko lawo. Imeneyo inali ntchito yaikulu ya ungwazi. Izo sizimafaniziridwa kawirikawiri, ndipo sizinayambe zaposedwapo, mdziko lino.

92 Koma, oh, icho chinali chinthu chaching’ono kwa chimene chinadzachitika tsiku lina! Pamene mtundu wa Adamu unaima, ziwanda zikugubira mkati kuchokera kumbali iliyonse, aneneri anali atalephera, lamulo linali litalephera, nsembe za ng’ombe ndi anaankhosa zinali zitalephera, chirengedwe cha munthu chinali chitalephera, chirichonse. Ndipo mtundu wawung’ono wa Adamu unaima, utagonjetsedwa; utaposedwa mchiwerengero ndi adierekezi, matsenga, matenda, nthenda. Analipo Mmodzi amene anatulukira kuchokera Kumwamba, ndipo anati, “Lero Ine ndiwufera mtundu wa Adamu.” Iye anabwera ku dziko lapansi ndipo anadzasanduka thupi. Iye anayang’ana pansi pamene mkati mwa mikondo panali pa mdima. Pa mdima kwambiri pamene munthu amapawopa panali pa imfa, ndipo Iye anaitengera imfa mchifuwa Chake. Ndipo pa Kalvare Iye analipira nsembe, ndipo anakuwa, “Ndikupanga njira kwa Ufulu!”

93 Ndipo Iye akufuula kwa Mpingo Wake, “Tengani Ichi chimene Ine ndakusiyirani inu, Magazi Anga ndi Mzimu Wanga, ndipo mumenye ndi chirichonse chimene inu muli nacho.” Ife tikhoza kugonjetsa usikuuno, kupyolera Chimenecho, mzanga. Inu mukhoza kumuthamangitsa mdierekezi kuti achoke kwa inu. Mdani wakale aliyense amene ali mu moyo mwanu, iye akhoza kuthamangitsidwa ndi Magazi ndi Mzimu wa Khristu, ndipo inu mukhoza kuima wangwiro mu Kukhalapo Kwake. Khristu anapanga njira!

94 Kodi inu mungathe kuchita zochuluka monga kukwezera nkono wanu kwa Iye, ndi kuti, "Mundikhululukire ine"? Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Wina wakenso, "Mundichitire ine chifundo, Mulungu, ine tsopano ndikuvomereza zolakwa zanga"?

95 Kodi alipo mamembala ena ofunda a mpingo amene amapita ku tchalitchi tsiku ndi tsiku, ndipo mwinamwake amayesera kukhala auzimu mmene angathere, komabe inu mukudziwa kuti kupsyamtima ndi kusayanjanitsika, ndi umbombo, zizolowezi zimakukokerani inu pansi mpaka inu simumakhala ndi chigonjetso? Kodi inu mungafune kuti muyeretsedwe ndi Magazi, usikuuno, kwa zonse zimenezo? "Pakuti wopembedzayo akatsukidwa kamodzi samakhalanso ndi chikumbumtima . . . " Kodi inu mungafune kuti mukweze dzanja lanu, inu membala wa mpingo? Mulungu akudalitseni inu, dona. Kwezani manja anu ndikuti, "M'bale Branham, mundikumbukire ine mu pemphero." Mulungu akudalitseni, dona. Uko nkulondola. Izo ndi zenizeni . . . Ndicho chinthu chenicheni choti muchite. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, bwana.

96 Winanso kwezani dzanja lanu, ndikuti, "Mundichitire ine chifundo, Mulungu. Ine ndikudziwa ine ndimadzinenera Chikhristu, koma ine sindimachikhala moyo icho. Ine ndikudziwa ine sindimatero. Ndipo mu mtima mwanga, ine ndithudi sindiri bwino ndi Inu. Ine ndikufuna kuti ndikhale mmodzi wa osankhidwa a Mulungu. Ine ndikumverera mu mtima mwanga kuti ine ndiri, koma ine sindinayambe ndaikapo kumbali zinthu zimene sizimachedwa kundifooketsa ine. Ndipo ine ndikufuna ndiziike izo kumbali usikuuno. Ndipo, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndichita zimenezo. Mundipempherere ine." Kodi inu mungakweze dzanja lanu? Mulungu akudalitseni inu, dona. Winanso. Pang'ono chabe, ife tikudikirira.

97 Pamene ife tikudikirira mwakachetechete, aliyense tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa mu pemphero, mofewa muzing'ung'uza iyi tsopano.

Kuli Kasupe wodzadza ndi Mwazi,
Wochokera mmitsempha ya Emanuele,
Ndipo ochimwa akagwera mkati Mwake . . .
Ataya zoipa, ataya . . .

98 Kodi inu simuganizira bwino bwino izo tsopano? Musayesere kuti muzisambe izo. Khristu ali mdzanja lanu.

99 Pilato anayesera izo, mmawa uno, cha pafupifupi sikisi koloko; koma manja ake akadali amagazi panobe, magazi ochimwa. Inu mukudziwa chimene chinamuchitikira iye. Iye anapita ku Switzerland, zaka zambiri kenako, anachita misala, anakadziponyera yekha kuti afe mu dziwe la madzi. Mmawa uno, ku Switzerland, mazana a anthu amabwera kuti adzawone malowo, madzi a buluu amabwata kuchokera pansi pa chidzenje

chachikulu icho cha madzi. Iwo amachita izo chaka ndi chaka. Ndi nkhani yotchuka yakale, iwo amati Mulungu anakaniza madzi kuti ayeretse manja ake.

100 M'bale, ziribe kanthu kaya mwabatizidwa kangati, chirichonse chimene inu mukuyesera kuti muchite, palibe chimene chiti chidzayeretse manja anu koma Magazi a Khristu. Mulungu anazikana izo. Ndipo madzi a buluu, zitatha zaka thuu sauzande, pafupifupi, amabwatabe. Mulungu amazikana izo. Chirungamo chanu chanu sichingathe kuyeretsa machimo anu. Si china koma Magazi a Yesu! Taganizani za zimenezo tsopano. Ife tipemphera, mphindi chabe.

101 Ine ndikudabwa ngati ine ndingafunse chinachake usikuuno. Pamene Iye anaima pamenepo mu holo ya chiweruzo cha Pilato, mmawa uja, ndipo anati, "Ngati Ufumu Wanga ukadakhala wa dziko lino, ine ndikanayankhula kwa Atate Anga ndipo pomwepo Iye akananditumizira Ine magulu thwelofu a Angelo." Pamene, mmodzi wa iwo akanakhoza kuwononga dziko. "Ine ndikanayankhula ndi Iye, ndipo magulu thwelofu a Angelo akadakhala pamenepo kuti Ine ndiwatume." Iye akanatha kuchita zimenezo. Koma Iye anaima pamenepo, wofatsa ndi wodzichepetsa, kuti atenge imfa yanu ndi kutenga machimo anu.

102 Kodi inu mungakhale oyamikira mokwanira chifukwa cha Nsembe imeneyo usikuuno, inu amene mukusowa zimenezo, ndi osowa madalitso a Mulungu, kodi inu mungaime pa mapazi anu kwa pemphero ili? Ingoimani pa mapazi anu, inu amene mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero ili, mukuti, "Mulungu, mundichitire ine chifundo. Ndine wolakwa, ine ndachita zinthu molakwitsa, ndipo tsopano ine ndikufuna kuti ndivomereze chikhululukiro changa kudzera mwa Khristu Yesu." Kodi inu mungabwere pamapazi panu basi pa nthawi ino? Mulungu akudalitseni inu, dona wamng'ono. Ndiko kulimbamtima. Ingokhalani chiimire pamenepo.

103 Kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti inu munakweza dzanja lanu, ndipo mutatero simukukhala woonamtima mokwanira kuti muime pamapazi anu? Kodi ndi chabwino chanji chimene Uthenga wakuchitirani inu? Oh, kusewera ndi mpingo kotero, kusewera ndi Mulungu! Ora posachedwapa lifika, limodzi la masiku awa bomba la atomiki lidzagunda cha kuno kwinakwake, mu zimakina zazikulu za ufa izi. Sipadzakhala chidutswa chimodzi cha mphindi kuti uziganizire izo. Zidzakhala mochedwa kwambiri nthawi imeneyo, ndipo mwinamwake isanafike Isitara inayo, kapena ngakhale Isitara ino. Kodi inu simuima tsopano, ndikuti, "Mulungu, mundichitire chifundo ine, wochimwa. Ine tsopano ndikumuvomereza Khristu, podzipereka Yekha ngati chitetezero cha machimo anga. Ndipo mwa chisomo Chake, ndipo chisomo Chake chokha, ine ndikukhala mu Kukhalapo kwa Mulungu." Kodi inu

mungavomereze zolakwa zanu? Iye amene adzabisa machimo ake sadzachita bwino. Iye amene avomereza tchimo lake, adzapeza chifundo. Izo ziri ndi inu. Iye akuwona.

104 Tsopano, Ambuye athu Wodala, mu chiwerengero choikika usikuuno paima miyoyo itatu yodzimvera chisoni, mwamuna mmodzi ndi akazi awiri.

105 Pamene ine ndikulingalira, Ambuye, za Kalvare, pamene mmodzi kumbali imodzi, anati, "Ambuye, mundikumbukire ine pamene Inu mukubwera mu Ufumu Wanu"; winayo anati, "Ngati Inu muli ameneyo, mutilole ife tiwone chozizwitsa, mutitsitse ife pa mtanda ndipo mudzipulumutse Nokha." Ndipo winayo anati, "Mulungu, mundichitire ine chifundo." Ndipo mutu Wanu unapotolokera kumbali yake ya kumanja, ndikuti, "Lero iwe ukakhala ndi Ine mu paradiso." Koma Inu munakhala chete kwa winayo, chifukwa apo panalibe kulapa.

106 Ndipo, Atate Mulungu, ine ndikupemphera kuti awa mwinamwake . . . Ine ndikudalira kuti ndi atatu okhawo mchipindachi, amene akumverera kuti akusowekera kuvomereza zochimwa zawo. Koma kuti iwo adzera mnjira yokwanira mu zonse, njira ya mtanda. Muwakhululukire iwo, Ambuye, ndipo muwadalitse iwo. Iwo aima pano usikuuno; monga Inu munawaimira iwo, mu holo ya chiweruzo cha Pilato; pamene Inu munawaimira iwo, pakati pa Miyamba ndi dziko lapansi, pamene dzuwa linakalowa ndipo mwezi unalephera kupereka kuwala kwake, ndipo chinsaru cha mkachisi chinang'ambika pamwamba mpaka pansi. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwadalitse iwo ndipo muwapatse iwo zifundo Zanu, ndipo muwayeretse iwo ndi Magazi Anu. Ndipo muwabatize iwo ndi Mphamvu Yanu yoyeretsa, akalowe mu Thupi la Mwana Wanu Yemwe, Khristu Yesu, pamenepo iwo akasungidwa kwa nthawi ndi Kwamuyaya. Muwadalitse ena amene akumverera kuti ali bwino, kuti iwo anachita kale izi ndipo anatero. Ine ndikupempherera mdalitso uwu kwa iwo, mu Dzina la Khristu. Ameni.

107 Mulungu akudalitseni inu. Ndipo inu amene mwaima pafupi ndi iwo amene anaimirira, afikireni ndipo muwagwire chanza, winawake, ndi kuti, "Ambuye akudalitseni inu," ndiko kulondola, ngati dzanja la chiyanjano.

108 Ife tsopano tangochedwerapo pang'ono mu misonkhano yathu. Ndi angati amawakonda Ambuye Yesu, kwezani dzanja lanu? Ine ndikudabwa, mwa kachetechete tsopano, kapena mwachete basi monga ife tingathere, pokumbukira Iye yemwe ali wopezekaponseponse, Amene ali pano usikuuno, ngati ife tingathe kuimba mofewa.

Panali pamtanda paja pomwe Mpulumutsi
anafera,
Pansi apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;

Pomwe mtima wanga (pamene inu munachita chofunikiracho, munaika manja anu pa Icho), pamenepo ku mtima wanga Magazi anapakidwa;
Oh, ulemerelo kwa Dzina Lake!

Tiyeni tiyimbe mofewa tsopano, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kwa Iye.

Pamtanda paja pomwe Mpulumutsi anafera,
Pansi apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;
Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;
Ulemerelo kwa Dzina Lake!

Ulemerelo kwa Dzina Lake, Dzina lofunika!
Ulemerelo kwa Dzina Lake lofunika!
Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;
Ulemerelo kwa Dzina Lake!

109 Tsopano mwakachetechete, ndi mitu yanu yoweramitsidwa. Inu amene mwapulumutsidwa, kuti, "Oh. . ." Mukweze dzanja lanu tsopano.

Oh, Kasupe wofunika wopulumutsa ku tchimo!
Ndine wokondwa kwambiri kuti ndalowamo;
Pamenepo Yesu anandipulumutsa ndipo amandikhalitsa woyera;
Ulemerelo kwa Dzina Lake!

Ulemerelo kwa Dzina Lake lofunika!
Ulemerelo kwa Dzina Lake lofunika!
Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;
Ulemerelo kwa Dzina Lake!

110 Tsopano ndi manja anu pansi, mitu yanu yoweramitsidwa. Ine ndinangoganiza; winawake anaimba mphindi pang'ono zapitazo, ndipo anati winawake amafuna kuti akumbukiridwe usikuuno mu pemphero, kwa thupi lawo. Iwo alephera kuti abwerere ku msonkhano wa Lamlungu usiku, kwa msonkhano wa machiritso wawukulu. Kodi inu mungaime ku mapazi anu, inu amene mukufuna kuti mukumbukiridwe mu pemphero limenelo tsopano?

. . . ku mtima wanga Magazi anapakidwa;
Ulemerelo kwa Dzina Lake!
Ulemerelo kwa. . .

111 Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa. "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zanu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwanu, chikwapu cha mtendere wanu chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake inu munachiritsidwa."

Ulemerelo kwa Dzina Lake!

112 Tsopano, Atate Wodala, pamene ife modzichepetsa tikuyandikira mtanda pakali pano, kumene chisomo ndi

chifundo zinandipeza ine, kumeneko Nyenyezi Yowala ndi ya Nthanda zimapereka kuwala Kwawo pa ine. Odwala awa aimirira mu Kukhalapo Kwanu. Iwo akukhulupirira pakali pano, kuti mwa chikhulupiriro, iwo akuyang'ana pa nsana wokwapulidwa uja, uko. "Ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa." Atate Woyera kwambiri, ife tikubwera tikuvomereza chikhulupiriro chathu, kukhulupirira kuti Inu muchiritsa matupi athu odwala, kudzera mu kuvutika kokhudza kwa Ambuye Yesu. Ndipo ife tikuwaperekera anthu awa amene aimirira, pemphero la chikhulupiriro, limene Inu munalonjeza kuti lidzamupulumutsa wodwala. Ndipo ife, palimodzi, ngati mtolo wa okhulupirira Anu usikuuno. Inu munati, "Paliponse pamene awiri kapena atatu adzasonkhana, Ine ndidzakhala pakati pawo." Ndipo ife tikuwapemphera iwo chifundo, kuti chisomo Chanu tsopano chikakhudze solo ya mkati-kati mwawo, kuti chinachake chikazikike mwakuya kwambiri; kuti iwo akathe kudziwa kuti Khristu ali pano ndipo wayankhula ndi iwo, kuti, "Mwana wa Ine, Ine ndatengera kudwala kwako kutali ku Kalvare. Tsopano basi ingoika nkhawa zako pa Ine, pakuti Ine ndimakusamalira iwe." Ndipo mulole iwo akachiritsidwe, chidutswa chirichonse chikakhale champhumphu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

113 Ndipo pamene iwo akukhala pansi tsopano, winawake wa pafupi ndi iwo, muike manja anu pa iwo, winawake amene amawapempherera iwo. Baibulo linati, "Iwo adzaika manja awo pa odwala; iwo adzachira." Ambuye akudalitseni.

114 Ngati ine sindikulakwitsa, kodi ine sindikuyang'ana pa munthu yemwe anachiritsidwa kuno masiku pang'ono apitawo, kapena ma Lamlungu angapo apitawo, yemwe anali wogontha kapena chinachake mmakutu? Ine ndikuwona kuti inu mukusangalala ndi msonkhano usikuuno. Inu mukundimva ine bwino bwino tsopano? Izo nzabwino. Zodabwitsa! Ingoimirirani ku mapazi anu mphindi chabe. Ndi angati akumukumbukira iye kuti anali kuno? Ndipo iye anadutsa pa mzere wa pemphero, anamubweretsanso iye mpaka pa nsanja, ndipo Ambuye anamuchiza iye ndipo anamupanga iye kukhala bwino. Adalitsike Ambuye! Zikomo inu, m'bale, chifukwa cha umboni wanu. Iwo ukhoza kukhala kudutsa madazeni! Koma kodi Iye si wodabwitsa?

115 Tsopano, ife tikufuna kuti tidzakuwoneni inu mawa usiku, molawirira. Ndipo kenako Lamlungu mmawa, molawirira. Lamlungu madzulo, ndipo ngati inu mungabwerere chifukwa cha msonkhano wa machiritso Lamlungu usiku. Mpaka ife tidzakomane, mulole ife tiime ndipo tiimbe nyimbo yathu yobalalitsira, "Tenga Dzinalo La Yesu Ndi Iwe."

Tenga Dzinalo la Yesu ndi iwe,
Mwana wosaukawe;

Ilo lidzakusangalatsa ndi kukutonthoza . . .
(Mupotolokere kumanja ndi kugwirana chanza tsopano ndi aliyense.)
Litengere Ilo kulikonse upita.

Dzina lofunika, (mupotolokere kumanja ndipo mugwirane chanza), O, kukoma kwake!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina lofunika, Dzina lofunika, O kukoma kwake! Kukoma kwake!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

Tsopano tayang'anani mbali iyi.

Pa Dzina la Yesu kuwerama,
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.

Dzina lofunika, O kukoma kwake! O kukoma kwake!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O kukoma kwake! Kukoma kwake!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

116 Tsopano mukumbukire kwayala ya a Neville, kuwulutsa kwa oyimba anayi mmawa, WLRP, naini koloko. Ndipo M'bale Stricker adzabwera pa naini-forte-faifi, Lamlungu mmawa. Timangopanga tepi ya iye madzulo ano, ya chiwukitsiro.

117 Ndipo tsopano, mpaka ife tidzakomanenso, madalitso a Ambuye akhale ndi inu, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu. Ndipo ine ndimupempha mzanga wabwino ndi m'bale, M'bale Palmer, wochokera ku Macon, Georgia, ngati iye angabalalitse msonkhano uno mu mawu a pemphero, pamene ife tikupemphera. M'bale Palmer.

Ungwiro CHA57-0419
(The Perfection)
Maulaliki a chitsitsimutso cha isitara

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham unalalikidwa mu Chingerezi pa Good Friday usiku, Epulo 19, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mu chaka cha ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2018 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

Voice Of God Recordings, Malawi Office
P.O. Box 51453, Limbe, Malawi

Voice Of God Recordings
P.O. Box 950, Jeffersonville, Indiana 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org